# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE

## NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NYENGO MSABATAYI

## KUYAMBIRA PA 6 APRIL MPAKA PA 12 APRIL, 2026

### NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Tiyembekezere nyengo ya mitambo ya patalipatali ndi mvula yamphamvu yamabingu ipitirira m'madera ochepa makamaka a mphepete mwanyanja ya Malawi, monga ku Karonga kuyambira Lolemba pa 6 April mpaka Lachitatu pa 8 April 2026.

Lachinayi pa 9 April 2026, tiyembekezere nyengo yamphepo, yozizira komanso mvula yomwe ikhonza kufalikira m'madera ena achigawo chakumwera komanso pakati koma yamphamvu m'madera ochepa a mphepete mwanjanja.

Mvulayi idzapitilira kugwa m'madera ochepa makamaka a mphepete mwanyanja mpaka kumapeto kwa sabatayi. Izi zikhala chomwechi kamba ka mphepo zochokera kumvuma komanso kumwera chakumvuma.

Tikuyembekezeranso nyengo ya mphepo ya mphamvu nthawi zina pa nyanja zonse makamaka nyanja ya Malawi.





Figure 1: Mlingo wa mvula omwe okuyemebekezeka msabatayi kuyambira 06th April to 12th April 2026

### NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Masiku anayi apitawa kuyambira pa 1 mpaka pa 4 April 2026, Mvula ya mphamvu inagwa m'madera ochepa akumpoto mphepete mwa nyanja ya Malawi makamaka ku Karonga ndi Nkhatabay. Mvula ya masiku amenewa inagwa yoposa mulingo wa mvula wa mwezi wonse wa April.

**Ku Kaporo north mvula ya masiku amenewa inagwa yokwana 404.5mm, motsogozana Kasantha komwe inagwanso ya mulingo wakwana 351.1mm ndipo Kabalelyamayolo inagwa yokwana mulingo wa 219.7mm.**

**Kagwedwe ka mvula kotereka, kaposa kwambiri mulingo wa mwezi wonse wa April wa 173.1mm. Izi zikutanthauza kuti mulingowu waposa ndi 233.7%, 202.8% komanso 126.9% m'masiku folowa.**





*Figure 2: Cummulative rainfall exceeding 50mm reported between 01st to 04th April 2026*

**UNDUNA WA ZACHILENGEDWE**

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

**LANGIZO:**

**Mphepo ya mphamvu pa nyanja:** ogwiritsa ntchito Nyanja akhale osamala.

***For further information please contact:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo otsindikiza: Blantyre** **Tsiku losindikiza: Lamulungu pa 5 April, 2026.**